

Mulungu Anachiritsa Hezekiya

Malangizo: Chitani zotsatirazi muli pamalo opanda phokoso. Pamene mukuwerenga mavesiwa, yerekezani kuti mukuona zinthuzo zikuchitika. Mukhale ngati mukumva zimene anthuwo akulankhula ndiponso mmene akumvera mumtima mwawo.

Amene akutchulidwa kwambiri m'nkhaniyi: Hezekiya, Yesaya

Chidule cha nkhaniyi: Hezekiya atadwala, anapemphera kwa Mulungu ndipo anachiritsidwa.

1

GANIZIRANI ZIMENE ZINACHITIKA.—WERENGANI YESAYA 38:1-9.

Fotokozani zimene mukuganiza pa za mmene Hezekiya anapempherera. (*Werenganinso vesi 3.*)

Kodi mukuganiza kuti mawu a Yesaya ankamveka bwanji pamene ankalankhula uthenga wochokera kwa Yehova wopezeka pa Yesaya 38:5-8?

Kodi mukuganiza kuti Hezekiya anatani Yesaya atamuza kuti achira matenda akewo?

2

FUFUZANI MOZAMA.

Kuwonjezera pa matenda akewo, kodi mukuganiza kuti n'chiyaninso chomwe chinkadetsa nkhwana kwambiri Hezekiya? (Zokuthandizani: Werengani Yesaya 36:1; 38:6.)

Kodi n'chiyani chimene mwina chinachititsa kuti Yehova amvetsera pemphero la Hezekiya? (Werengani 2 Mbiri 31:20, 21; Yesaya 38:3.)

N'chifukwa chiyani ziyenera kuti zinali zovuta kuti Yesaya abwererenso kwa Hezekiya ndi uthenga wosiyana ndi zimene analosera poyamba?

Kodi mukudziwa bwanji kuti kubwerera m'mbuyo kwa mthunzi kunalidi chozizwitsa chenicheni, osati zinthu zongoganizira? (Werengani 2 Mbiri 32:24, 31.)

3

GWIRITSANI NTCHITO ZIMENE MWAPHUNZIRA.

Lembani zimene mwaphunzira zokhudza . . .

Mtima umene Yehova ali nawo wofunitsitsa kumvetsera mapemphero athu.

Zimene munthu angachite kuti adzikonedwa ndi Mulungu.

4

DZIFUNSENI KUTI:

Ndi zochitika ngati ziti pa moyo wanga zimene nthawi zonse ndiyenera kumapemphera kwa Yehova?

Kodi ndingatani kuti mapemphero anga azikhala abwino komanso ochokera pansu pa mtima?

M'nkhaniyi, kodi ndi mfundo iti imene yandikhudza mtima kwambiri, ndipo n'chifukwa chiyani?

Mungachite izi: Yerekezani kuti ndinu mtolankhani ndipo mukupereka lipoti la nkhaniyi pa wailesi kapena pa TV. Fotokozani zimene zinachitika ndipo mufunse mafunso anthu amene akutchulidwa m'nkhaniyi komanso amene anaona pamene zinthuzo zinkachitika.



Koperani nkhaniyi
pa www.jw.org